MFUNDO ZINA ZA ULOSI

Phunziro 1, April 5, 2025



"Koma ngati munthu akufuna kunyadira, anyadire chinthu ichi: kuti iye amamvetsa za Ine ndipo amandidziwa, kuti ndine Yehova, amene ndimakonda chifundo, chilungamo ndiponso ungwiro pa dziko lapansi. Zimenezi ndizo ndimakondwera nazo," akutero Yehova"

Yeremiya 9:24

Zizindikiro, mawu osamveka bwino, kufananitsa, komanso zachilendo zomuchitikira m’mneneri... Umu ndi mmene ulosi wa m’Baibulo uliri.

Ena salabadirakonse kuyesera kuti amvetse tanthauzo lake, ndipo amakhala okhutira ndi zomwe wina angawauze. Ena amatenga ndime imodzi kapena ziwiri ndi kupanga matanthauzo odabwitsa opanda gwero lenileni.

Koma omwe amawerenga ndi kumvetsetsa molondola amakula mu chidziwitso chawo cha Mulungu ndi kulandira madalitso ochuluka. Kodi ndi mfundo ziti zomwe zingatithandize kuphunzira ndi kumvetsa ulosi wa m’Baibulo moyenera?



- **Mfundo Yoyamba:** Werengani ndi mtima woyenera.
- **Mfundo Yachiwiri:** Zindikirani mutu waukulu.
- **Mfundo Yachitatu:** Gwiritsirani ntchito kafukufuku.
- **Mfundo Yachinayi:** Kumvetsetsa nkhani yonse mwa thunthu.
- **Mfundo Yachisano:** Kumvetsetsa tanthauzo la zizindikiro.

MFUNDO YOYAMBA: WERENGANI NDI MTIMA WOYENERA

"Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mau a chinenerocho, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira. (Chivumbulutso 1:3)

Pali dalitso kwa amene amawerenga ulosi (Chiv. 1:3a). Koma, ndi ochepa kwambiri amene amamva kuti amadalitsika powerenga maulosi amene ali m'buku la Chivumbulutso, Danieli, Yesaya, Zekariya, ndi ena.

Ndichifukwa chiyani zimenezi zimachitika? Chifukwa samawerenga maulosiwo ndi malingaliro woyenera. Pamene Yesu anati, "Wowerenga azindikire" (Mateyu 24:15), ankatiuza kuti tiri ndi kuthekera komvetsetsa, koma potsatira zinthu zina zofunika :

Khalani okonzeka kumvera zimene ulosi umatiphunzitsa (Chivumbulutso 1:3)

Tiyenera kuzindikira kuti tiribe nzeru zokwanira zomvetsa maulosiwa, koma timadalira nzeru zaumulungu kuti timvetse (Mateyu 11:25; Yereremiya 9:23)

Kuwerenga ulosi kuti ndifotokozere maganizo anga okhudza mmene zinthu zina zidzachitikira, kapena osamva mawu a Mulungu m'maulosimo, si njira yoyenera.



MFUNDO YACHIWIRI: ZINDIKIRANI MUTU WAUKULU

"ndi kuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu" (2 Timoteyo 3:15)

Olemba Salimo anavomereza kuti sanathe kumvetsetsa mozama za nzeru za Mulungu, popeza nzeru za Mulungu ndi zopanda malire (Masalimo 139:6; 147:5). Paulo akutiuza kuti zochita za Mulungu ndi "osasanthulika," kutanthauza kuti ndizosatheka kufufuza ndi kumvetsetsa (Aroma 11:33)

Momwemonso, ndi zosatheka kuti ife timvetsetsa malingaliro a Mulungu, monganso mmene ziliri kuti ife tigwire mwezi ndi manja athu (Yesaya 55:9.)

Mwa ubwino, Mulungu wapanga kuthekera kodzitsitsa kufika pa mlingo wathu potithandizira kumvetsetsa zina za maganizidwe Ake. Mu Baibulo, Mawu a Mulungu, ngakhale munthu ochepetsetsa m'maganizidwe kwambiri, atha kuona kuona chikondi cha Mulungu ndinso chipulumutso chomwe Iye akutipatsa (2 Tim. 3:15).

Ndondomeko ya Chipulumutso ndiyo mutu Mfundo yaikulu ya Baibulo, indedi, ya maulosi amene ali m'menemo.

MFUNDO YACHITATU: GWIRITSIRANI NTCHITO KAFUKUFUKU

"Koma iwe Daniele, tsekera mau awa, nukomere chizindikiro buku, mpaka nthawi ya chimaliziro; ambiri adzathamanga chauko ndi chauko, ndi chidziwitso chidzachuluka" (Daniel 12:4)

Pamodzi ndi lamulo loti atseke buku – kubisa zomwe ziri mmenemo – mpaka nthawi yotsiriza, Danieli anauzidwa za kuwonjezeka kwa chidziwitso cha kafukufuku-chidziwitso chofunikira – kuti amvetsetse ulosiwo (Danieli 12:4).)

Pamene Yesu anasadulika munthu, chisindikizo chimenechi chinayamba kusweka. Maulosi ena a Danieli anayamba kumveka (Mateyu 24:15). Pambuyo pake, maulosi ena anawonjezedwa olembedwa m'buku "losasindikizidwa": Chivumbulutso (Chiv. 22:10)

Mu 1798, pamene Napoleoni anathetsa ulamuliro wa Papa umene unalamulira mwamphamvu kwa zaka zambiri, anthu ambiri anaona izi ngati kukwaniritsidwa kwa maulosi a Danieli. Mulungu anali atatsegula buku la Danieli kwathunthu, ndipo anapereka chidziwitso chofunikira kuti anthu amvetse ulosiwo.

Simaulosi okha amene anayamba kumveka bwino kuyambira nthawi imeneyo, komanso mitu ina monga Sabata komanso kumvetsetsa za iwo amene anafa, zinayambanso kumvetsedwa molondola.

Tiyeni tifunse Wolemba maulosi kuti atipatse nzeru ndi kafukufuku wofunikira kuti timvetse maulosi ake.

MFUNDO YACHINAYI: KUMVETSETSA NKHANI YONSE MWA THUNTHU

"Ndipo kuyambira ndi Mose ndi aneneri onse Iye anawafotokozera zimene zinalembedwa m'malemba wonse zokhudzana ndi Iye mwini" (Luka 24:27)

Kuwerenga maulosi paokha mosagwirizanitsa ndi nkhani yonse kumabweretsa kutanthauzira kochititsa kaso, kosagwirizana konse ndi matanthauzo enieni a ulosiwo.

Yesu anatiphunzitsa kuti tiphunzire Baibulo mwachimango chonse, ndiye kuti, tilione ngati chinthu chimodzi chathunthu (Luka 24:27)

Kutenga gawo limodzi lokha (mwachitsanzo ulosi) ndi kumanga mfundo potengera gawo limenelo lokhalo, ndi njira yolakwika yophunzira Mawu a Mulungu. Njira yolondola ndikufanizira malembawa ndi ena omwe amayankhuliranso mu mutu womwewo m'magawo osiyanasiyana a Baibulo.

Mfundo ina yofunika kuiganizira ndi nkhani yonse ya malembawo, ndiye kuti, nkhani yozungulira lemba linene likuphunziridwa. Kodi malemba amene ali patsogolo ndi pambuyo pake akunena chiyani? Ndani analemba, linali liti, ndipo chifukwa chiyani?

Kutenga lemba popanda kuyang'ana nkhani yake yonse kungapangitse kuti limanene chilichonse chimene tikufuna, koma osati chowonadi chimene likufuna kutiphunzitsa.

MFUNDO YACHISANO: KUMVETSETSA TANTHAUZO LA ZIZINDIKIRO

"Tanthauzo la nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene waziona m'dzanja langa lamanja ndi la zoyikapo nyale zagolide zisanu ndi ziwiri ndi ili: Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndi angelo a mipingo isanu ndi iwiri ija, ndipo zoyikapo nyale zisanu ndi ziwiri zija ndi mipingo isanu ndi iwiri ija" (Chivumbulutso 1:20)

Maulosi a m'Baibulo ali odzadza ndi zizindikiro ndi zithunzi. Nthawi zochepa, ulosiwo umalongosola tanthauzo lake (Danieli 8:20; Chivumbulutso 1:20). Koma, nthawi zambiri, tanthauzo lake lake silifotokozedwa.

Kuyesa kutenga zithunzi zimenezi mmene ziliri ndikupanda nzeru. Yesu alibe lupanga lakuthwa mbali ziwiri lotuluka m'kamwa mwake (Chivumbulutso 1:16)

Kuti timvetse zizindikirozi, tiyenera kuyang'ana magawo ena a Baibulo kumene maganizo ofanana kapena zizindikiro zofananazo zagwiritsidwa ntchito. Tiyeni tione zitsanzo zina :

Kodi nyanga za chirombo choopsa mu Danieli 7:7-8 zikutanthauza chiyani?

Ndimafumu komanso maufumu omwe iwo amaimirira(Danieli 7:24; 8:21)

Kodi lupanga lakunthwa lotuluka mkamwa mwa Yesu Chivumbulutso 1:16 likutanthauza chiyani?

Baibulo (Aefeso 6:17; Ahebri 4:12)

Kodi mkazi otchulidwa mu Chivumbulutso 12:1 ndi ndani?

Anthu okhulupilira Mulungu (Aefeso. 5:31-32; 2 Akorinto. 11:2)

Mulungu watsimikizira kuti aliyense amene akufuna kumvetsa maulosi adzatha kuwamvetsa.

“Zilibe kanthu kuti munthu wapita patsogolo bwanji munzeru, asaganize ngakhale kwa kanthawi kuti palibe chifukwa chofufuzira mozama ndi mopitiriza m’Malemba kuti apeze kuwala kochuluka. Monga anthu a Mulungu, timayitanidwa payekha-payekha kukhala ophunzira a maulosi. Tiyenera kukhala tcheru ndi mtima wonse kuti tidziwe kuwala kulikonse kumene Mulungu angatipatse. Tiyenera kugwira kuwala koyamba kwa choonadi; ndipo kudzera mu kuphunzira ndi kupemphera, kuwala kowonekera bwino kungapezeke, komwe kungaperekedwe kwa ena.”

EGW (Testimonies for the Church, volume 5, page 708)